JW.ORG™
Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

Dziwani Zoona Zokhudza Mulungu

Werengani Aroma 10:13-15. Anthu amaphunzira kuitana pa dzina la Yehova, Akhristu akawalalikira uthenga wabwino. Pitani patsamba loyamba la pa jw.org kuti muone mmene anthu mamiliyoni ambiri akulalikirira "uthenga wabwino wa zinthu zabwino."

Nonse monga banja, onani chithunzi chilichonse chimene chaikidwa patsamba loyamba, pamwamba. Yesani kuganizira kuti ndi cha dziko liti. Kenako dinani pamene alemba kuti "TSEGULANI" kuti muone ngati yankho lanulo ndi lolondola komanso kuti mudziwe chiwerengero cha anthu a Mboni za Yehova amene akuphunzitsa ena uthenga wa m'Baibulo m'dzikolo. Mukatero onani pamapupo ndipo muloze dziko limene inuyo mukukhala.

▶ **TSOPANO YESANI IZI:** Sankhani dziko limodzi pa mayiko amene asonyezedwa patsamba loyamba la pa jw.org. Pogwiritsira ntchito zinthu zofufuzira zimene muli nazo, fufuzani zinenero zimene zimalankhulidwa m'dzikolo. Pitani pagawo lakuti "Mabuku" pa jw.org ndipo yesani kupeza chinenero chimodzi mwa zinenero zimene mwapezazo. Mukasankha chinenerocho, dinani batani lakuti "Fufuzani." Ngati chinenerocho chapezeka, koperani buku ndiponso zinthu zomvetsera kuti muone mmene chinenerocho chimaonekera komanso mudziwe mmene chimamvekera.

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania